Baibulo ya ana

Ikupasilani

Mfumu
Yokongola
Yopusa

Yolembedwa ndi: Edward Hughes

Yojambulidwa ndi: Janie Forest
Alastair Paterson

Yotengedwa ndi: Lyne Doerksen

Yotathauzidwa ndi: Tapiwa Maraira

Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

©2022 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.

Samuele, woweruza ndi mtsogoleri wa Israeli anali wokalamba. Anaika ana ake aamuna kuti akhale oweruza a Isiraeli kuti alowe m'malo ake potumikira Yehova. Koma ana a Samuele anali oipa. Iwo ankakonda ndalama ndipo ankagwiritsa ntchito mphamvu zawo kuti apeze ndalama mwachinyengo.

Aisiraeli anavutika chifukwa cha kuipa kwa mwanayo. Makhoti anali opanda chilungamo. Anthu ankayenera kulipira ana a Samuele nthawi iliyonse imene ankafuna thandizo.

Chinachake chinayenera kuchitidwa. Tsiku lina akulu a Isiraeli anasonkhana n'kupempha Samuele kuti awathandize.

“Tipatseni mfumu kuti itiweruze,” akuluwo anapempha motero. Iwo sanafune kuti ana oipa a Samuele awaweruze. Iwo ankafuna mfumu mofanana ndi mitundu yonse yowazungulira.



Samuele anakwiya. Israyeli anali ndi Mfumu kale! Mulungu Wamphamvuyonse, Wamuyayayo, analamulira Israyeli. Kalekale, Iye anawamasula ku ukapolo ku Igupto, kuwatsegulira Nyanja Yofiira kuti apulumuke.


Kenako anapatsa Aisiraeli
dziko lawo lokongola.

Pamene Samuele anapemphera, Yehova anati: “Iwo sanakane iwe, koma anandikana Ine, kuti ndisakhale mfumu yawo; iwo atumikira milungu ina.”



mfumu yawo ya
padziko lapansi
idzatenga ndalama
zawo m'misonkho;
kudzithandiza
yekha ku minda
yawo yabwino ndi
minda yamphesa;
lamulirani ana awo
aamuna m'magulu
ankhondo ake; ndi
kuwauza ana awo
aakazi kuti
amgwire ntchito.

MUNDA WA MPESA WA CHIFUMU
KHALANI PANJA
Koma anthu ankafunabe mfumu.

Mulungu adatsogolera Samuele kwa mnyamata wokongola kwambiri, wamanyazi kwambiri, komanso wamtali kwambiri - wamtali kwambiri kuposa wina aliyense. Dzina lake anali Sauli. Samuele ataona Sauli, Yehova anati, Uyu adzakhala mfumu ya anthu anga.

Momvera, Samuele anadzoza Sauli kukhala mfumu ya Israyeli. Pamene iye anaonetsa Sauli kwa ana a Israyeli, iwo anapfuula, Mfumu ikhale ndi moyo wautali!

Posakhalitsa Mfumu Sauli anayesedwa. Aamoni, omwe ankadana ndi Aisiraeli, anazungulira mzinda wa Aisiraeli ndipo anaopseza kuti achotsa diso lamanja la munthu aliyense. Ndi dongosolo lankhanza bwanji!



Nkhani yoopsayi inafika kwa Mfumu Sauli. Iye anakonzekeretsa ankhondo ake.



Pamene magulu ankhondo aŵiriwo anakumana, Sauli anawononga Aamoni ndi kupulumutsa mzindawo. Mfumu Sauli anapatsa Mulungu ulemerero, nati: “Lero Yehova wachita chipulumutso mwa Israyeli!”

Mulungu anapatsa Sauli chipambano chachikulu tsiku limenelo. Koma sikuti Sauli ankalemekeza Mulungu nthawi zonse. Tsiku lina, asanamenyane ndi Afilisti, Sauli anapereka nsembe kwa Mulungu.



Iye ankadziwa kuti imeneyo inali ntchito ya Samuele. Iye akhadziwa kuti Mulungu akhafuna kuti iye adikhire mpaka Samweli mbabwera kudzacita pyenepi. Koma Sauli sanamvere Mulungu!

Samuele atafika, anauza Sauli kuti: “Wachita zopusa. Sunasunge malamulo a Yehova Mulungu wako.” Sauli ayenera kuti ankaganiza kuti linali tchimo laling’ono. Koma kusamvera Mulungu n’koopsa nthawi zonse.

Pa nthawi ina, Mulungu anauza Sauli kuti awononge anthu oipa a ku Amaleki. Koma Sauli ndi anthuwo anasiya Agagi mfumu ya Amaleki.



Ankasunganso zinthu zamtengo wapatali, nkhosa ndi ng'ombe. Sauli ananena kuti anasunga zinthu zimenezi kuti apereke nsembe kwa Yehova.

Samuele anauza Sauli kuti: "Kumvera ndi bwino kuposa nsembe." Sauli anamva chisoni kwambiri ndi tchimo lake. Koma zinali mochedwa kwambiri. Moyo wake wonse unali wosasangalala chifukwa sanamvere Yehova.

Mfumu Yokongola Yopusa

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

1 Samuele 8-16

"Polowela pa mau anu pamapasa kuwala."
Masalimo 119:130

Mapeto

Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16